NYA_TTB_0916_20161003_script

**Danieli : 1:2-13**

**Mutu : Danieli asankha kukhala wokhulupirika kuukapolo.**

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyeni tiyambe ndi mau apa Hoseya 4:6, akuti, “Anthu anga aonongeka chifukwa cha kusadziwa; popeza unakana kudziwa, Inensondikukaniza, kuti usakhale wansembe wanga.”

Mupologalamu yapita, tinali kusanthula Danieli 1:1, pa nkhani ya Chiyambi cha bukuli, kugwa kwa ufumu wa Yuda ndi kuonongeka kwa Yerusalemu. Ndipo lero pa Danieli 1:2-13, tiona kuti, Danieli akusankha kukhala wokhulupirika ku ukapolo.

2. Ndipo Yehova anapereka Yehoakimu, mfumu ya Yuda, m’dzanja lake, pamodzi ndi zipangizo zina za m’nyumba ya Mulungu, namuika nazo iye ku dziko la Sinara, ku nyumba ya mulungu wake, nalongazipangizozo m’nyumba ya chuma cha mulungu wake.

Poyamba ndifuna kunena mau akuti, pamene Yehoakimu anamangidwa panali ganizo lakuti atengedwe ndi kupitanaye ku Babulo monga mwa mau apa 2 Mbiri 36:6, koma pazifukwa zina,

sanatengedwe kotero kuti anafera mu Yerusalemu, ngakhale sanaikidwe mwaulemu. Ichi, ndichimene Yeremiya 22:18-19, akunena kuti, “Chifukwa chake Yehova atero za Yehoakimu mwana wa Yosiya, mfumu ya Yuda: Sadzamlira iye, kuti kalanga ine m’bale wanga! kapenakalanga ine, mlongo wanga! Sadzamlira kuti kalanga ine mbuye! kapena kalanga ine ulemerero wake! Adzamuika monga kuika buru, adzamkokanadzamponya kunja kwa zipata za Yerusalemu.”

Tsono mwina inu mukufunsa kuti, pamene tiwerenga 2 Mbiri 36:6, tipeza mau akuti, “Nebukadnezara mfumu ya ku Babulo anakwerakuyambana naye, nammanga ndi matangadza kumuka naye ku Babulo.”Koma taonani mkulu wina wotchedwa Jahn, akunena kuti ichi, chikhoza kukhala cholakwika chomwe chinalowam’menemu popeza palibe umboni wakuti Yehoakimu anali ku Babulo. Ndipo pa 2 mafumu 24:1-2, tikumva kuti Yehoakimuanakhalabepaufumuali pansipaulamuliro wa Nebukadnezara kwa zaka zitatu. Ndiye tikunena kuti palibe chifukwa chakuti tinene kuti m’buku la Mbiri muli cholakwa ayi, koma chilungamo ndichakuti panali ndithu cholinga chofuna

kumutenga ndi kupita naye ku Babulo, koma pazifukwa zina zokhudza ufumu wa ku Babulo, anasintha.

Tsono pamene Nebukadnezara anadzanso kuononga Yerusalemu, anatenga zipangizo zina za m'Kachisi popeza anali ndi cholinga chofuna kupanga Yuda kukhala ufumu pansi wa ulamuliro wake. Ndiye tikumva kuti Nebukadnezara anatenga zipangizozi m'dziko la Sinara, lomwe ndi dzina lakale la Babulo (Gen.11:2, Yesaya 11:11; Yeremiya 5:11). Iye, anafuna kukaikazipangizozi mu kachisiwamulungu wake, wotchedwa Beli. Tere, tiyenitigwiritsitse mau amenewa chifukwa Belsazara ndiye adzaziturutsazipangizozi patsiku la phwando lake.

3. Ndipo mfumu inauzaAsipenazimkuru wa adindo kuti abwera nawo ena a ana a Israyeli, a mbeu ya mafumu, ndi ya akalonga;

Pano pali chithunzi chakuti Nebukadnezara anali kusankha ndi kutenga anthu ofunika okha-okha, kupitanawo ku Babulo. Ambiri a iwo anali anthu a nzeru popeza ndiwo amene anali kupereka uphungu kwa mfumu Nebukadnezara.

Tsono Danieli ndi anzake atatu aja, ndiwo amene anali kutumikira m'nyumba yachifumu, koma anawapanga kukhala wosakhala ndi ana.Ichi, ndichifukwa chake tikumva kuti Danieli anali osakwatira komanso analibe ana.Koma pamene tikamba kuti Danielianamuononga kuti sanakhale ndi ana, sitikunena kuti anaonongekansom'mutu ayi, koma kuti akhale womvera basi.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti anyamatawa akuzunzika chifukwa akulipa tchimo la makolo awo.Tere, anyamataokongolawaakutengedwa ndi mfumu ndi cholinga chofuna kusonyeza kuti iye ndiye wamphamvu.Komanso kuti pamene anawaali m'manja mwa mfumu makolo awo, akhale ndi makhalidwe abwino omvera ndi cholinga chakuti ana awo, asalandire nkhaza.  Ichi, ndichifukwa china anyamatawa anali kuphunzitsidwa mokwanira ndi cholinga chofuna kuonetsa chikondi cha mfumu pa iwowa.

4. Anyamataopanda chirema, a maonekedwe okoma, a luso la nzeru zonse, ochenjeram'kudziwa, a lunthalakuganizira, okhozakuimiriram'chinyumba cha mfumu; ndi kuti awaphunzitse m'mabuku ndi manenedweaAkasidi.

Ndime ino, ikunena kuti mfumu inali kusankhaanyamata, amene anali a zaka zapakati pa khumi ndi ziwiri, ndi khumi ndi zisanu, amene anali ndi maonekedwe okoma.Kutanthauza kuti maonekedwe okongola a thupi kunali kuganiziridwa kuti munthu anali wanzeru ndi wamphamvu m'mutu mwake.Kutsimikiza kuti anyamata amene anapatsidwa udindo wotumikira m'nyumba yachifumu, amayenera kukhala anzeru komanso ooneka bwino.Ichi, ndichifukwa china chomwe anyamatawa anali kuphunzitsidwa mokwanira ndi cholinga chakuti atumikire ndi kukhala aphindu ndi kutengera ulemu ku dzina la mfumu.

Anyamatawa amayenera kukhala anzeru za maphunziro a dziko lawo monga momwe Mose anaphunzitsidwa maphunziro a ku Aigupto.Momwemonso Danieli anaphunzitsidwa maphunziro ya Akasidi, amene anamuthandizira kukhala ndi nzeru zoposa pa zauzimu.  Iyi, ndiyo nkhani yomwe ili pa Danieli 1:17, pamene akuti, "Koma anyamata amene anayi, Mulungu anawapatsa chidziwitso ndi luntha la m'mabuku ali onse, ndi nzeru; koma Danieli anali nalolunthа la m'masomphenya ndi maloto onse." Tere, tikuphunzira kuti anthu amene amachita bwino m'moyo uno,

amayenera kuphunzira akali pamsinkhu waung'ono, umene munthu amaphunzira.Kutsindika kuti ngati msinkhu uwu, upitilira ndiye kuti kuphunzira kumakhala kobvuta.Tere ndichinthu chochititsa chisoni kuti anthu ochuluka, amene akanagwira ntchito zofunika, koma pano sakudziwika chifukwa chosapatsidwa mwayi wolandira maphunziro okwanira.Nebukadnezara anasankhaanyamata anzeru ndi kuwaphunzitsamokwanira, ndi cholinga chakuti akhoze kukhala ophunzira bwino.

5. Ndipo mfumu inawaikira gawo la chakudya cha mfumu tsiku ndi tsiku ndi la vinyo wakumwa iye, ndi kuti awalere zaka zitatu, kuti potsiriza pake aimirire pamaso pa mfumu.

Pano tikuona mtima wachifundo womwe Nebukadnezara waonetsakwaanyamata a chi Yuda. Ndikunena mau amenewa chifukwa chakuti anyamatawa anali akapolo. Tsono Nebukadnezara poonakabadwidwekaanyamatawo, moyo wawo ndi nzeru zawo,anawachitira chifundo ndi kuwalemekeza kuti ukapolo wawo uyende bwino.

Koma taonani Danieli ndi anyamata anzake, anali wochokera ku pfuko la Yuda, kotero kuti anakulandichiphunzitso cha chilamulo

cha Mose.Kotero kuti kunali kobvuta kuti anyamata awa, alandire ndi kudya chakudya choperekedwa kumafano. Mwanjira ina Danieli ndi anzake anali kudziwa nyama, mbalame ndi nsomba zina zomwe sizimayenerakudyedwa. Koma pofuna kuwaiwalitsa Mulungu wa makolo awo, anyamatawa anapatsidwa maina a chilendo, kusiya mayina awo amene analandira panthawi ya mdulidwe.Tikunena kuti ngakhale anyamatawasanaumilizidwe kuti asiye chipembedzo cha makolo awo, koma zinthu zomwe anali kuwachitira, zikutsimikizadi kuti amafuna kuti anyamatawo asiye chipembedzo chawo.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna mutsegule maso anukunzeru imeneyi masiku ano.Mukaonetsetsamupeza kuti palibe munthu amene angakuumirizeni kutsatira chipembedzo chake, koma zochitika za m'dziko lino, zikusonyeza kuti inu muyenera kutsatira chipembedzo cha satana.Lero, satana akunena kuti simuyenera kusiya chipembedzo chanu, koma mumvale ndi kuonetsa makhalidwe onse osalemekeza Mulungu wanu. Mwanjira ina inu mukhoza kupita ku church chanu, kuchita zonse zofunika kumeneko, koma mtima wanu usaperekedwe kwa Ambuye. Tere

ndichifukwa chake akristu ambiri ndi achipembedzo chokha, koma alibe Yesu mumtima mwawo.Kodi inu, ndinu m'modzi mwa otere?

6. Mwa awa, tsono munali a ana a Yuda, Danieli, Hananiya, Misayelindi Azariya.
7. Ndi mkuruwaadindoanawapatsa mayina ena; Danieli anamutcha Belitsazara; ndi Hananiya, Sadrake; ndi Misayeli, Mesaki; ndi Azariya, Abedinego.

Pano tikuona kuti mkuluwaanyamatawaakusintha mayina awo, achiHebri ndi kuwapatsa mayina achikunja. Danieli akumupatsa dzina la Belitsazara, lomwe litanthauza wopembedzafano la Baal.Kenaka Hananiya kukhala Sadrake, Misayeli kuti ndiye Mesaki ndipo Azariya kukhala Abedinego.

Tsono mwina inu mwafunsa kale kuti, kodi panali chifukwa chanji kuti mayina aanyamata aja, asinthidwe? Yankho likuti, anyamata awa, anali ochokera ku Yuda, amene mayina awo anali achipembedzo chawo, kotero kuti kusintha uku, inali njira imodzi yofuna kuti ayiwale Mulungu wawo, dziko lawo komanso chikhalidwe ndi miyambo yawo. Mwanjira ina, amafuna

anyamataawa, kuti ayambekupembedzamulungu wawo komanso kuti asakhale alendom'gulu la anthu, omwe anali kuwatumikirawo.

Taonani Danieli akupatsidwa dzina la mulungu wawo, ndi cholinga chakuti apereke chithunzi chakuti anali wokondedwa ndi chipembedzo komanso mulungu wawo.Iyi, inali njira yachinyengoyofunakumukopa kuti apatukepachikhulupiriro chake cha Mulungu oona.

Wokondedwa anzanga apaulendo, mayina onse achikunjawa zikutanthauza kuti Nebukadnezara wapambana ndi kugonjetsa Mulungu wa a Yuda, koma osadziwa kuti kunali kugwa kwa ufumu wake. Leronso alipo anthu ambiri achikunja, amene amaganiza kuti akupambanamzochita zawo, koma ikudza nthawi pomwe Mulungu adzaoneka kuti ndiye Wamphamvuyonse.

8. Koma Danieli anatsimikiza mtima kuti asadzidetse ndi chakudya cha mfumu, kapena ndi vinyo amamwa; chifukwa chake anapemphamkuruwaadindoamloleasadzidetse.

Danieli mundime ino akuonetsa kulimba mtima pachikhulupiriro chake cha pa Mulungu wake, ngakhale anali m'dziko

lachilendo.Taonani akuchita izi, osati ali ndi cholinga chofuna kumveka, kapena kuti akondweretse Nebukadnezara ayi. Kutsimikiza kuti Danieli analibe ganizo lomwe akristu ambiri masiku ano achita.Taonani akristu aleroamayendera mwambi wakuti, ukapita ku Roma, uzichita zomwe a Roma achita.Kutsimikiza kuti Danieli analibe mtima wachinyengo monga ambiri tirinawo.Kusonyeza kuti anali ndi chikhulupiriro cholimba pa Mulungu wake, komanso analibe mtima wadyera monga wokhulupirira ambiri alinawo.  Kunena kuti Danieli ngakhale anali m'dziko, koma sanali wadziko, popeza anali atasinthikamwakukonzekakwa maganizo ake, kotero kuti kufuna kuchita chifuniro cha Mulungu ndicho chinali pamtima pake.  Kodi inu mulinachochikhumbokhumbo chofuna kuchita chifuniro cha Mulungu?

Tsono Danieli ndi anyamata anzake akuimira gulu lochepa la anthu okhulupirika, amene amapezekamum'badwo uliwonse.  Ili, ndilo gulu la anthu wotsala lomwe Paulo akulinena pa Aroma 11:5, pamene akunena kuti, “Choteronso nthawi yatsopanochiripochotsalira monga mwa kusankha kwa chisomo.”

Tsopano tikuona kuti anyamata awa, sakufuna kudya chakudya cha mfumu, kumene kuli kugalukira cholinga cha mfumu Nebukadnezara. Komabe pali ganizo lakuti anyamatawaawadzaze ndi mtima wakuti ndiwo anthu aku Babulo, ngakhale m'maonekedwendi kabvalidwekawo. Koma Danieli ndi anzake, ndiwo amene anaphunzitsidwamokwanira chilamulo cha Mose chakuti sayenera kudzidetsa ndi zakudya wamba. Mwanjira ina amayenera kusungachiyero monga Yehova anena pa Levitiko 11:44-47, kuti samayenera kudzidetsa ndi zakudyazodetsedwa ndipo kuti amayenera kukhala woyera monga Mulungu ali woyera. Mwanjira inaanyamataawa, anamva ndi kumvetsetsauphungu wa Yesaya 52:11, pamene anati, "Chokani inu, chokani inu, turukani ku Babulo; musakhudze kanthu kodetsa; turukani pakati pake, khalaniokonzeka, inu amene munyamulazotengera za Yehova." Tere pano anyamataachiHebriwa akuonetsa chithunzi choimapamalamulo a Mose, kumene kuli kuima pa Mulungu wawo.Kodi inu mukhoza kuima pa Mulungu wanu motere?

9. Ndipo Mulungu anamkometsera Danieli mtima wamkuru wa adindo, amchitire chifundo.

Ndime ino, ikunena kuti Danieli anaoneka wokoma m'maso mwa mkuluwam'dindo. Izi, zinachitika ndi Mulungu mwanjira yomwe anaika, monga muja Yosefe anakondedwanso ndi mkuluwoyang'anirakaidi. Kutsimikiza kuti kukonderedwa kwa anthu a Mulungu ndi anthu achikunja, kumachokera kwa Mulungu. Taonani pa Genesis 39:21, akunena kuti, "Koma Yehova anali ndi Yosefe namchitira iye zokoma, nampatsa ufulu pamaso pa woyang'anirakaidi." Komanso pa Masalmo 106:46, tipeza kuti Israeli naye anakonderedwa kudzera mwa Mulungu. Tamvani; akunena kuti, "Ndipo anawachitira kuti apezensoni pamaso pa onse amene adawamanga ndende."

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani iyi, ikulinga pa mau akuti, "Njira za munthu zikakomera Yehova, ayanjanana naye ngakhale adani ake." Kutanthauza kuti pamene wokhulupiriraalim'chiyanjano ndi Yehova, amapezanso m'dalitso m'ngakhale pamaso pa adani ake. Koma tiphunziranso kuti pamene ana a Mulungu ali mu Babulo, kapena kuti m'dziko lapansi, ayenera kusamalitsa kuti asatengeke ndi uchimo wa m'dzikolo.

10. Nati mkuruwaadindo kwa Danieli, Ine ndiopambuyanga, mfumu amene anakuikirani chakudya chanu ndi chakumwa chanu; pakuti aonerenji nkhope zanuzachisoni zoposa za anyamataolingana ndi inu? momwemomudzaparamulitsa mutu wanga kwa mfumu.

Tamvani mkuruwaadindo pano, akunena kuti ngati Danieli ndi anzake, adzaonekewoonda, wachisoni, komanso wosaoneka bwino monga momwe mfumu amayembekezera, zidzakhala kuti iyeyu sanamvere malamulo a mfumu. Komansochidzaonetsa kuti mkuru uyu, ndiye akudyachakudyachi, kotero kuti sichikufikakwaanyamatawa.Ndiye mwakutero moyo wake, udzakhalapachiswe.Apa, ndipo pamene mkuru uyu, anakhala kakasi, kuti kodi achita chiyani pamenepa?

11. Nati Danieli kwa kapitao, amene mkuru wa adindo adamuikayo ayang'anire Danieli, Hananiya, Misayeli ndi Azaliya.

12. Muyesetuanyamata anu masiku khumi; atipatsezomeram'nthakatidye, ndi madzi timwe.

Danieli mundime ino, akumuuza mkuruwoyang'aniraanyamata aja, awayesekwa masiku khumi, ndi zakudya wamba ndipo aone ngati pangakhale kusintha koipa kwa matupi awo.Kunena kuti nthawi yomwe anaperekayi ndi yokwanira kuti zakudyazozionetse ngati ziri zoyenera kapena ayi.Koma taonani kuti zotsatira zake zinali zokondweretsa, popeza matupi ya anyamata aja, anaonekaathanzi, amphamvu komanso okongola.

13. Pamenepo mupenye maonekedwe athu ndi maonekedwe aanyamataakudya chakudya cha mfumu; ndi monga umomuonera, muchitireanyamata anu.

Danieli akunenetsa kuti, mkuruoyang'aniraanyamatawoasadere nkhawa ndi moyo wake, popeza pakapita masiku ochepa, aona kusinthikakwamatupi awo. Pano tikuona kuti Mulungu wabweretsa m'dalitso pa mkuruyu, umene upite kwa Danieli ndi anzake.

Ndiye ndifuna muone kuti nthawi zina malamulo omwe amaikidwam'zipembedzo zathu sakhala othandiza konse, koma kupsinja anthu ena.Takumbukirani Ambuye Yesu anadzudzula Afarisi pa Luka 11:39, kuti, "Tsopano inu Afarisi muyeretsa kunja

kwake kwa chikho ndi m'bale, koma m’kati mwanu mudzalazolanda ndi zoipa.” Kutanthauza kuti Afarisi anali ndi chizolowezichosamalira maonekedwe akunja, osati mkati mwa munthu ayi.Ichi, ndicho chipembedzo chonyenga. Ndiye Paulo akumuuza Tito 3:5, kuti, “Zosati zochokera m’ntchito za m’chilungamo, zimene tidazichita ife, komatu monga mwa chifundo chake anatipulumutsa ife, mwa kutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwea Mzimu Woyera.” Mau awa, akutanthauza kuti ndikosatheka kuchita ntchito zabwino kapena kuyenda m’moyo wachiyero, pokhapokha munthu abadwensokwatsopano, kumene kumachokera Kumwamba.

Tere, tikutsiriza ndi mau akuti, Danieli kuti afikepokanazakudya za m’nyumba yachifumu, ndiye kuti anagwiritsitsa chikhulupiriro choona cha Mulungu wamoyo. Kutsimikiza mau ya Ambuye Yesu akuti, ife tiri m’dziko lapansi, koma sindifeadziko lapansi ayi. Kutanthauza moyo wathu uyenera kukhala woyera monga Mulungu ali woyera.

Lero tilekeza pano ndipo timasanthulaDanieli 1:2-13, momwe taona Danieli akusankha kukhala wokhulupirika ku ukapolo.

Ambuye akudalitseni inu lero.  Amen!